

Mfundo Zothandiza Pogwira Ntchito Zachitukuko M'mayiko Osiyanasiyana

Zokhudza Nkhaniyi Komanso Mmene Zimagwirira Ntchito:

Mliri wa COVID-19 wachititsa kuti boma la Scotland liunikenso mmene limachitira zinthu pothandiza ndi ntchito zachitukuko mayiko amene akukwera kumene pa nkhani zachuma. Kuwonjezera pamene, zochita za gulu lomenyera ufulu wa miyoyo ya anthu akuda (*Black Lives Matter*) zachititsa kuti boma la Scotland lisinthe zina n'zina. Zimenezi zachititsa kuti bungwe lotchedwa *Scottish Government's International Development* lisinthe mfundo zake zokhudza mapulogalamu othandiza mayiko omwe akukwera kumene pa nkhani ya chuma chifukwa zinthu zikusintha mofulumira kwambiri padziko lonse.

Masomphenya (ID ya Ndondomeko ya 2016)

Masomphenya a boma la Scotland adakali akuti kudzera m'ndondomeko ya mfundo za Bungwe la United Nations, dziko la Scotland lipitiriza kuthandiza pa nkho yolimbana ndi umphawi, zinthu zopanda chilungamo, ndiponso nkho yolimbana ndi katangale padziko lonse.

Mfundo Zothandiza: Bungwe la *International Solidarity* ndi loima palokha ndipo limathandiza pa nkhani zokhudza ufulu wachibadwidwe wa anthu padziko lonse. Ife timagwirizana ndi bungweli pogwira ntchito zathu zonse. Timamenyela ufulu wa anthu komanso timafotokoza maganizo anthu momveka bwino, mokoma mtima ndiponso mwachilungamo. Timachita zimenezi pamene tikulimbikitsa ufulu wachibadwidwe, ufulu wa demokalase ndiponso pamene tikulimbikitsa kumvera ndi kutsatira malamulo.

Pulogalamu yathu imathandiza ndondomeko zotsatirazi:

1. Zitukuko zimene mayiko akuchita: tikuzindikira kuti dziko lililonse lili ndi ntchito zimene limaona kuti n'zofunika kugwiridwa mwachangu pa nkhani ya chitukuko ndipo mayikowo amayika ntchitozi pamalo oyamba. Choncho ife timathandizira ntchito zoterezi popereka ndalama. Timaonetsetsanso kuti tikuthandiza mayikowo m'njira zosiyanasiyana, kuphatikizapo kuwatumizira akatswiri ndi akadaulo odziwa bwino kugwira ntchitozo omwe amaphunzitsa amisiri a m'mayikowo kuti azigwira ntchitozo mwaukadaulo. Kuchita zimenezi kumathandiza kuti n'kupita kwa nthawi, mayikowo akhale odziimira paokha pa chuma ndiponso pa ntchito za chitukuko, zomwe zikuphatikizapo ntchito zothandiza anthu pakachitika ngozi zadzidzidzi zachilengedwe.

2. Kuchita zinthu mopanda tsankho: tikudzindikira kuti tsankho ndiponso kusiyana kwambiri pa nkhani zachuma kwakhala kulipo kuyambira kalekale, choncho ife tikufunitsitsa kuthetsa mavuto amenewa pa kagwiridwe kathu ka ntchito. Sitigwirizana ndi tsankho la mtundu uliwonse ndipo timalimbikitsa kuti pamalo athu a ntchito, pasakhale tsankho ngakhale pang'ono. Timalimbikitsa kwambiri ufulu wa amayi ndi atsikana, ndipo timawathandiza kuti azikhala ndi mwayi wofanana ndi azibambo.

3. Kuthandiza kuti mawu a anthu osauka azimvedwa: padziko lonse, timalimbikitsa ndiponso kuthandiza anthu osauka ndiponso oponderezedwa n'cholinga choti mawu ndi madandaulo awo azimveka.

4. Anthu osiyanasiyana azitenga nawo gawo m'ntchito zosiyanasiyanso: timatha kupereka mafunso kwa anthu ndi akatswiri omwe timayamikira ntchito zawo, timamvetsera maganizo awo, komanso timaonetsetsa kuti anthu audindo akugwira ntchito yawo motsatira malamulo. Timalimbikitsanso ndi kuthandiza anthu omwe ali ndi maganizo atsopano amene angathandize pa ntchito zosiyanasiyana, komanso timamvetsera

madandaulo a anthu omwe nthawi zambiri amakhala ndi mfundo zatsopano zomwe zingathandize kusintha zinthu.

5. Kugwirira ntchito limodzi: timapanga mgwirizano ndiponso ubale ndi anthu omwe ali ndi mfundo ndiponso masomphenya othandiza. Anthu amenewa amakhala ochokera m'mayiko osiyanasiyana omwe timagwiramo ntchito ndipo izi zimathandiza kuti tizitha kugawana nzeru, upangiri ndi masomphenya, zomwe zikugwirizana ndi mgwirizano umene timapanga pa msonkhano wathu wa mu 2016 wotchedwa *International Development Strategy* pa mfundo yotchedwa "*Beyond Aid agenda*".

6. Upangiri watsopano ndiponso kusintha zinthu: timakonza mapulogalamu omwe ndi: osavuta kuwatsatira ndiponso kuwasintha, ogwiritsa ntchito ndalama ndi zipangizo zochepa koma othandiza ngakhale zinthu zitasintha mwadzidzidzi; mapulogalamu omwe m'kupita kwa nthawi, sawononga chilengedwe, amathandizira kuti chuma chikwere, komanso amakhala ndi ndondomeko yabwino yoyenera kutsatira ngati patachitika mavuto a mwadzidzidzi. Tikuzindikiranso kuti padziko lonse lapansi pali mavuto amene akuyamba chifukwa cha kusintha kwa nyengo, choncho tikulimbikitsa ndi kuthandizira pa mapulogalamu amene angagwirebe ntchito bwino ngakhale pali kusintha kwa nyengoku, ndipo timaonetsetsa kuti aliyense akumvetsa bwino zoyenera kuchita. Izi zimathandiza kuti aliyense aziona kuti ntchito ikuchitika mwachilungamo, mopanda tsankho, ndiponso m'njira imene ngakhale anthu a m'mayiko osauka akhoza kukwanitsa kutenga nawo mbali.

7. Luso la makono: timathandizira mapulogalamu okhudza luso la makono pa nkhani ngati zaumoyo, zachitukuko ndiponso zosamalira chilengedwe. Zimenezi zingaphatikizepo kulandira thandizo pogwiritsa ntchito zipangizo zamakono m'malo mochita kuyenda kuti munthu akalandire thandizolo kutali. Pamene tikuchita izi, timazindikiranso kuti si onse amene angakwanitse kupeza thandizo pogwiritsa ntchito luso la makono, makamaka anthu a m'mayiko osauka.

8. Kuchita zinthu poyera, mopanda chinyengo ndiponso m'njira yosavulaza ena: ife a boma la Scotland pamodzi ndi mabungwe amene timagwira nawo ntchito timachita zinthu poyera ndiponso mopanda chinyengo ndipo timayankha kwa anthu a m'madera amene tikuwatumikira komanso timayankha ku dziko la Scotland. Timaonetsetsa kuti ntchito yathu yonse ikugwiridwa motsatira malamulo ndiponso mfundo zothandiza kupewa ngozi. Timaonetsetsanso kuti ntchito yeniyeniyo singavulaze anthu ena.